# PHUNZIRO LA 38

1. Kodi pamene a Isirayeli analibe madzi, iwowo ana-khulupilira mwa Mulungu kuti aŵapatsa madzi?
-Iyayi.

2. Kodi chifukwa chiyani Mulungu analankhula kwa Mose ndi Aroni kuti iwowo sadzaloŵa mu dziko la Kanani?
-Chifukwa chakuti iwowo sanamumvere Mulungu.
-Chifukwa chakuti Mose anakantha tanthwe m'malo mo-yankhula kwa tanthwelo.

3. Chifukwa chakuti a Isirayeli anapitirizabe kudandawu-la, kodi Mulungu anaŵachitira chiyani a Isirayeli?
-Mulungu anaŵalanga a Isirayeli, poŵatumizira njoka za ululu zambiri .

4. Kodi njokazo zikufanana bwanji ndi tchimo?
-Tchimo limaŵaluma anthu ngati m'mene zinaŵalumira a Isirayeli njoka za ululu zija ndi kufa.

5. Kodi Mulungu anamuwuza Mose kuti achite chiyani pofuna kuŵapulumutsa a Isirayeli?
-Anamuwuza kuti apange njoka ya mkuwa ndipo ayi-pachike pa mtengo.

6. Kodi a Isirayeli amene amkafuna kuti apulumuke, amayenera kuchita chiyani?
-Kuyang'ana pa njoka ya mkuwa imene anayipachika pa mtego ija.

7. Kodi a Isirayeli onse amene anayang'ana pa njoka ya mkuwa imene anayipachika pa mtengo ija, anafa?
-Iyayi.

8. Kodi njoka ya mkuwa ija, inali ndi mphamvu zina zili-zonse zoŵapulumutsira a Isirayeli?
-Iyayi.

9. Kodi ndani yekha amene anali ndi mphamvu zoŵapu-lumutsira a Isirayeli?
-Mulungu.

10Kodi tchimo la a Isirayeli linayitanitsa imfa?
-Inde.

11. Ngakhale kuti tchimo la a Isirayeli linayitanitsa imfa pakati pawo, kodi Mulungu anachita chiyani kwa anthu amene anamukhulupilira Iye?
-Mulungu anaŵapulumutsa iwowo.

-Chifukwa chakuti a Isirayeli sankamukhulupilira Mulun-gu, iwowo sanaloŵe mu dziko la Kanani.

-Chifukwa chakuti a Isirayeli sankamukhulupilira Mulun-gu, iwowo ankangozungulirazungulira mchipululu kwa zaka zokwana 40, mpaka pa nthaŵi imene akulu akulu onse anafa.

-Kodi chifukwa chiyani Mulungu anaŵapatsa chilango a Isirayeli?
-Chifukwa chakuti a Isirayeli anakana kukhulupilira mawu a Mulungu amene Mose anabweretsa kwa iwowo.

-Ine ndikufika kwa inu ndi mawu a Mulungu ngati m'mene anafikira Mose ndi mawu a Mulungu kwa a Isirayeli.

-Ngati inu muli ngati a Isirayeli, okana mawu a Mulungu, Mulungu adzakulangani inu ngati m'mene anaŵalangira



-Kodi Mulungu anamuwuza chiyani Samuyele?
-Mulungu anamuwuza Samuyele kuti a Isirayeli sankamukana Samuyeleyo.

-Mulungu anamuwuza Samuyele kuti, chifukwa chakuti a Isirayeli ankafuna mfumu, iwowo ankamukana Mulun-gu ngati mfumu yawo.

-Mulungu anaŵapatsa a Isirayeli mfumu.

Tiyeni tiŵerenge 1 Samuyele 11:14-15

14-Chomcho Samuyele anaŵawuza anthuwo kuti, “Tiyeni tipite ku Giligali, kumeneko tikasankhe mfumu.”
15-Chomcho anthu onse anapita ku Giligali ndipo analengeza ndikumusankha Sawulo kukhala mfumu pa maso pa Ambuye. Kumeneko anapereka msembe kwa Ambuye, Sawulo ndi a x onse anali pa chikondwelero chachikuru.

-Ngakhale kuti a Isirayeli anamukana Mulungu ngati mfumu yawo, Mulungu anaŵapatsa iwowo mfumu yina.

-Dzina lache ndi Sawulo.

-Sawulo anali mamuna woyamba kukhala mfumu wa a Isirayeli.

kapatsidwa chakudya ndi madzi m’chipululu muja?
-Mulungu.

-Kodi Mfumu ya a Isirayeli inali ndani pamene iwowo ankapatsidwa dziko la Kanani?
-Mulungu.

-Kwa zaka zambiri, Mulungu anakhala ali Mfumu ya a Isirayeli.

-Kuchokera mu nthaŵi imene Mulungu anaŵapulumutsa a Isirayeli ku ukapolo ku Iguputo kuja, Mulungu anakhala ali Mfumu yawo.

-Koma tsopano, a Isirayeli sakumufunanso Mulungu kuti akhale Mfumu yawo.

-A Isirayeli ankafuna kuti adzifanana ndi anthu oyipa amene anayandikana nawo, pokhala ndi munthu ngati mfumu yawo.

-A Isirayeli anamukana Mulungu ngati mfumu yawo.

-Apa pali zimene Mulungu ananena kwa Samuyele.

Tiyeni tiŵerenge 1 Samuyele 8:7-8a

7-Chomcho Ambuye anamuwuza Samuyele kuti, “Umvere zonse zimene akukuwuza anthuwo, sikuti akukukana iweyo, ayi, koma akundikana Ine ngati mfumu yawo.
8-Ngakhale pamene ndinaŵaturutsa ku Iguputo mpaka lero lino, anandisiya Ine ndikumayipembedza milungu ina.”



a Isirayeli.

-Patatha zaka 40, akulu akulu onse a a Isirayeli atafa, Mulungu anaŵatsogoleranso a Isirayeli mpaka m’malire a dziko la Kanani.

-Chifukwa chakuti Mose sanamumvere Mulungu, Mulungu sanamulore Mose kuti aŵatsogolere a Isirayeli polowa mu dziko la Kanani.

-Chifukwa chakuti Mulungu sanamulore Mose kuti aloŵe mu dziko la Kanani, Mulungu anasankha mtsogoleri watsopano kuti aŵatsogolere a Isirayeli.

Tiyeni tiŵerenge Numeri 27:18-20 ndi 22-23

18-Ambuye anati kwa Mose, “Umutenge Yoswa mwana wa Nuni amene ali ndi Mzimu, ndipo uyike manja ako pa mutu pache.
19-Umuyimitse pa maso pa Eliyazara wamkuru wamsembe ndi khamu lonse, ndipo umuloŵetse m’malo mwako onse akuwona.
20-Umupatse iye udindo wako wina kuti a x adzimumvera.”
22-Mose anachita zimene Mulungu anamulamula iye. Anamuyimika Yoswa pa maso pa Eliyazara wamkuru wa a msembe onse ndi khamu lonse.
23-Mose anayika manja ache pa iye ngati m’mene Mulungu anamulamulililira iye, ndipo anamupatsa udindo ngati oloŵa m’malo mwache.

-Kodi mtsogoleri watsopano wa a Isirayeli amene Mulungu anamusankha kuti aloŵe m’malo mwa Mose anali ndani?
-Yoswa.

-Yoswa atasankhidwa kuti akhale mtsogoleri watsopano wa a Isirayeli, Mulungu anamuwuza Mose kuti akwere pa phiri limene linali pafupi ndi malire a dziko la Kanani.

-Pamwamba pa phiri paja, Mulungu anamuwonetsa Mose dziko la Kanani limene analilonjeza kwa Aburahamu, Isaki ndi Yakobo, pamodzi ndi zidzukulu zawo.

Tiyeni tiŵerenge Dotolonomo 34:1-4

1-Mose anakwera pa phiri la Nebo kuchokera mu chigwa cha Mowabu mpaka pamwamba pa Pisiga, kuwoloka kuchokera ku Yeriko. Pamenepo Ambuye anamuwonetsa adziko lonse la Kanani kuchokera ku Giliyadi mpaka ku Dani,
2-mpaka ku Nafutari konse, malire a Eferemu ndi Manase, dziko lonse la Yuda mpaka kumadzuro kwa nyanja yayikuru,
3-ku Negefi ndi ku malire onse kuchokera ku chigwa cha Yeriko, mzinda wa migwalangwa mpaka kukafika ku zowari.
4-Ndipo Ambuye anati kwa iye, "Ili ndiye ndiye dziko limene ndinalilonjeza polumbira kwa Aburahamu, Isaki ndi Yakobo pamene ndinati, "Ndidzalipereka kwa zidzukuru zako." Ndakulora kuti angoliwona dzikoli ndi maso ako, koma siwuwomboka kuti akalilowê dziko limeneli."

-Chifukwa chakuti Mose sanamumvere Mulungu, Mulungu sanamulore Mose kuti alowê mu dziko la Kanani.

-Kodi Mulungu anasunga mawu ache osamulora Mose kuti alowê mu dziko la Kanani?



ne anakalowâ m'malo mwa Samuyele, a Isirayeli anasonkhana ndikupita kukamuchezetsa Samuyele.

Tiyeni tiŵerenge 1 Samuyele 8:4-6

4-Kenako akulu akulu a ku x anasonkhana pamodzi, ndipo anapita ku Lama kwa Samuyele.
5-Ndipo anamuwuza kuti, "Wakalamba ndiponso ana ako sakutsata khalidwe lako labwinoli. Tsopano usankhe munthu amene akhale mfumu yathu kuti ifenso tikhale ndi mfumu ngati m'mene alili mayiko enaŵa."
6-Koma atamuwuza kuti, "Mutipatse mfumu wakuti adzititsogolera ife, " izi zinamukwiyitsa Samuyele. Chomcho Samuyele anapemphera kwa Ambuye.

-Kodi a Isirayeli anamupempha kuti achite chiyani Samuyele asanamwalire?

-A Isirayeli anamupempha Samuyele kuti aŵasankhire mfumu kuti adziŵatsogolera.

-Kodi chifukwa chiyani Samuyele anakwiya ndi zimenezi?
-Samuyele anakwiya ndi zimenezi chifukwa chakuti a Isirayeli ankamukana Mulungu kuti akhale Mfumu yawo.

-Kodi Mfumu ya a Isirayeli inali ndani pamene iwowo anapulumutsidwa ku Iguputo kuja?
-Mulungu.

-Kodi Mfumu ya a Isirayeli inali ndani pamene ankatsogoleredwa m'chipululu muja?
-Mulungu.

-Kodi Mfumu ya a Isirayeli inali ndani pamene iwowo an-

-Chifukwa chakuti Mulungu anapereka lonjezo lakuti adzatumiza Mpulumutsi kudzera mu zidzukulu za a Isirayeli.

-Chifukwa chakuti Mulungu analonjeza kuti adzatumiza uthenga wache , Bayibulo, kupitira mu zidzukuru za a Isirayeli.

-Mulungu amafuna kuti anthu ache onse adzimvera uthenga wache kuti adzapulumutsidwe.

-Oweruza omaliza wa a Isirayeli amene Mulungu ana-musankha anali Samuyele.

-Samuyele anakhala ali Oweruza wa a Isirayeli kwa zaka zambiri.

-Samuyele atakalamba, panalibe wina aliyense amene anakatha kuloŵa m'malo ache, chifukwa chakuti ana a Samuyele anali osakhulupilira mwa Mulungu.

Tiyeni tiŵerenge 1 Samuyele 8:1-3

1-Samuyele atakalamba, anasankha ana ache ku-khala atsogoleri a a x.
2-Mwana wa Samuyele oyamba anali Jowelo, wachiŵiri anali Abija, iwowo ankalamulira ku Bereseba.
3-Koma iwowo sankatsatira zimene ankachita bambo awo. Ankakonda ndalama zokha, ankalandira ziphuphu kumbali ndipo sankaweruza bwino milandu chifukwa ankayimira mbali.

-Chifukwa chakuti Samuyele anakalamba kwambiri, ndiponso chifukwa chakuti panalibe wina aliyense ame-



-Inde.

-Nthaŵi zonse Mulungu amasunga mawu ache.
-Mulungu sadzaŵayiwala mawu ache.

-Mulungu atamuwonetsa Mose dziko la Kanani, Mose anamwalira.

Tiyeni tiŵerenge Dotolonomo 34:5

5-Ndipo Mose, wotumikira wa Ambuye anamwalili-ra komweko ku Mowabu ngati m'mene analankhulira Ambuye.

-Mose atamwalira, Mulungu analankhula kwa Yoswa.

-Mulungu anamuwuza Yoswa kuti akonzekere zoloŵa mu dziko la Kanani.

Tiyeni tiŵerenge Yoswa 1:1-2

1-Pambuyo pa imfa ya Mose, mtumiki wa Am-buye, Ambuye anamuwuza Yoswa, mwana wa Nuni, mtumiki wa Musa kuti:
2-"Mose, mtumiki wanga, wamwalira. Tsopano iwe pamodzi ndi anthu onse mukonzeke kuti muwoloke mtsinje wa Yorodani pokalowâ mu dziko limene ndikufu-na kuŵapatsa a x tsopano.

-Mose atamwalira, Yoswa anaŵatsogolera a Isirayeli ku-lowâ mu dziko la Kanani.

-Kodi Mulungu anasunga lonjezo lache ndikulipereka dziko la Kanani kwa zidzukulu za Aburahamu?
-Inde.

-Mulungu anapereka dziko la Kanani kwa a Isirayeli ngati m'mene anaperekera lonjezo kwa Aburahamu, Isaki ndi Yakobo.

-Sanata ndi Farawo anayesa kuŵasunga a Isirayeli mu ukapolo ku Iguputo.

-Koma Mulungu anasunga lonjezo lache lopereka dziko la Kanani kwa a Isirayeli.

-A Isirayeli sankakhulupilira kuti Mulungu angaŵapatse madzi ndi chakudya m'chipululu muja.

-Koma Mulungu anasunga lonjezo lache lopereka dziko la Kanani kwa a Isirayeli.

-Mulungu amasunga malonjezo ache nthaŵi zonse.
-Mulungu satha kuphwanya ngakhale lonjezo limodzi lokha.

Tiyeni tiŵerenge Yoswa 11:23a

23-Chomcho Yoswa analilanda dzikolo ngati m'mene Mulungu anamuwuzira Mose, ndipo analipereka kwa x malingana ndi mafuko awo.

-Tsopano a Isirayeli ankakhala mu dziko la Kanani.

-Pamene Yoswa anali ndi moyo, a Isirayeli ankamukumbukira Mulungu.

Tiyeni tiŵerenge Oweruza 2:7



moyobe, a Isirayeli ankamutsata Mulungu.

-Ngati Oweruza amene Mulungu amamusankha wamwalira, a Isirayeli amabweleranso koŵapembedza mafano aja m'malo mwa Mulungu.

Tiyeni tiŵerenge Oweruza 2:17-19

17-Koma a x sankaŵamvera Oweruza awo. A x anali osakhulupirika pa maso pa Ambuye ndipo ankayipembedza milungu ina. Makolo awo anaŵamvera malamulo a Ambuye, koma m'bado watsopanowu unasiya kutsatira zonsezi.
18-Mu nthaŵi zonse zimene Ambuye ankapereka Oweruza, Ambuye ankamuthandiza Oweruzayo ndipo ankaŵapulumutsa anthuwo kwa adani awo, Oweruzayo akakhala ali moyo. Ambuye amaŵachitira chisoni chifukwa cha kubuwula, kuvutitsidwa ndi kupsinjidwa.
19-Koma Oweruza akamwalira, anthu ankayambiranso kuchita zimene ankachita kale, mpaka kumaziposanso zimene ankachita makolo awo. Amkayitumikira milungu ina ndikumakana kusiya kuyipa kwawo.

-Ngakhale kuti Mulungu anaŵapatsa a Isirayeli chilango chifukwa cha tchimo lawo, Mulungu ankaŵakondabe ndipo ankaŵateteza a Isirayeliwo.

-Kodi chifukwa chiyani Mulungu ankaŵakondabe ndipo kuŵateteza a Isirayeli?

-Chifukwa chakuti Mulungu anapereka lonjezo kwa Aburahamu, Isaki ndi Yakobo kuti adzakhala ndi zidzukuru zambiri ndipo udzakhala mtundu wawukuru kwambiri.

-Chifukwa chakuti a Isirayeli anasiya kumupembedza Mulungu ndikumaŵapembedza mafano a Baala ndi Ashiroti, Mulungu anaŵapatsa chilango.

-Kodi Mulungu anaŵapatsa chilango chotani a Isirayeli chifukwa chopembedza mafano?
-Mulungu anatumiza adani a a Isirayeli kuti akaŵawonongere a Isirayeli mbewu zawo zonse.

-Mulungu anaŵatumiza adani a a Isirayeli kuti akabere a Isirayeli ziweto zawo zonse.

-Mulungu anaŵatumiza adani a a Isirayeli kuti akaŵapange a Isirayeli onse kukhala akapolo.

-A Isirayeli atavomereza kuchimwa kwawo, ndikumupempha Mulungu kuti aŵapulumutse, kodi Mulungu anachita chiyani?

Tiyeni tiŵerenge Oweruza 2:16

16-Kenako Ambuye anaŵapatsa a x Oweruza amene anaŵapulumutsa m'manja mwa adani awo okwera ma hachi.

-A Isirayeli ataŵavomereza machimo awo, ndikumupempha Mulungu kuti aŵapulumutse, Mulungu anasankha amuna ndi akazi mwa a Isirayeliwo kuti aŵatsogolere iwowo poŵagonjetsa adani awo.

-Amuna ndi akazi amene anasankhidwa ndi Mulungu kuti aŵatsogolere a Isirayeli kuti aŵagonjetse adani awowo, ankatchedwa kuti Oweruza.

-Ngati Oweruza amene Mulungu amamusankha ali



7-Anthu ankamupembedza Mulungu pamene Yoswa anali moyo, ndipo akulu akulu amene amkakhara momuyang'anitsitsa Yoswa, anaziwona zinthu zazikuru zimene Mulungu anaŵachitira a x.

-Patapita nthaŵi, Yoswa anakalamba ndipo anamwalira.

Tiyeni tiŵerenge Oweruza 2:8-9

8-Yoswa, mwana wa Nuni, mtumiki wa Ambuye anamwalira ali ndi zaka 110.
9-Ndipo anamuyika ku dziko limene anakalitenga, ku Timunati Helesi m'dziko la mapiri la Efelemu, kumpoto kwa phiri la Gaasi.

-Pamene Yoswa anali moyo, a Isirayeli ankamukumbukira Mulungu.

-Yoswa atamwalira, a Isirayeli anamukana Mulungu ndipo anali oyipitsitsa.

-Yoswa atamwalira, a Isirayeli anapanga mafano ndikumaŵapembedza mafanowo m'malo mwa Mulungu.

Tiyeni tiŵerenge Oweruza 2:10-13

10-Mtundu uli onse utasonkhana kwa makolo awo, mtundu wina unabuka, umene siwumaŵadziŵa Ambuye ngakhale zimene Ambuye anaŵachitira a x.
11-Kenako a x anachita zinthu zoyikwa kwambiri pa maso pa Ambuye poŵapembedza mafano a Baala.
12-Anaŵasiya Ambuye, Mulungu wa makolo awo, amene anaŵaturutsa mu dziko la Iguputo. Ankaŵatsatira ndiponso kumaŵapembedza mafano osiyanasiyana a anthu amene anayandikana nawo. Anamupangitsa

Mulungu kuti akwiye kwambiri
13-chifukwa anamutaya Iye ndikumamutumikira Baala ndi Ashiroti.

-Anthu amene anayandikana ndi a Isirayeli ku Kanani, ankapembedza mafano otchedwa Baala ndi Ashiroti.

-Chifukwa chakuti a Isirayeli anakana kumpembedza Mulungu, nawonso ankapembedza mafano a Baala ndi Ashiroti.

-Kodi ndani amene anaŵanamiza a Isirayeli kuti amukane Mulungu ndikumaŵapembedza mafano a Baala ndi Ashiloti?
-Satana.

-Satana anaŵanamiza anthu ndipo anthu ankaganiza kuti ankamupembedza Mulungu.
-Koma anthuwo sankamupembedza Mulungu, ayi.

-Anthuwo ankamupembedza Satana amene ankabisala m'mafano a Baala ndi Ashiloti.

-Ngati m'mene Satana anabisalira mwa njoka kuti amunamize Adamu ndi Hava, Satana ankabisalanso m'mafano a Baala ndi ashiroti kuti aŵanamize anthu.

-Satana amabisalanso mwa mizimu ndi mizimu ya makolo athu.
-Anthu akamapembedza mizimu ndi mizimu ya makolo athu, amaganiza kuti akumupembedza Mulungu.

-Koma samamupembedza Mulungu, ayi.
-Amakhala akumupembedza Satana.



-Ngati tikumpembedza wina wake kapena china chake osakhala Mulungu, kodi tikumupembedza ndani?
-Satana.

-Kodi chifukwa chiyani Satana amafuna kuti anthu adzipembedza mafano?
-Chifukwa chakuti Satana amamuda Mulungu, chomcho safuna kuti wina aliyense adzimupembedza Mulungu.

-Chifukwa chakuti Satana amaŵada anthu onse ndipo samafuna kuti Mulungu aŵapulumutse anthuwo.

-Kodi Mulungu ankadziŵa kuti a Isirayeli ankapembedza mafano a Baala ndi Ashiroti?
-Inde.

-Kodi Mulungu anakwiya ndi a Isirayeli poŵapembedza mafano a Baala ndi Ashiloti?
-Inde.

-Kodi Mulungu anachita chiyani kwa a Isirayeli?

Tiyeni tiŵerenge 2:14-15

14- Chifukwa chakuti Ambuye anali ndi mkwiyo ndi a x, anaŵalekelera adani awo okwera ma hachi ndiponso adani awo ena kuti aŵabere iwowo mbewu zawo ndiponso kuŵagulitsa ngati akapolo kwa adani awo amene anayandikana nawo mwakuti a x analephera kudziteteza okha.
15-Mu nthaŵi zonse zimene a x amapita kukamenya nkhondo, Ambuye ankalimbana ndi iwowo kuti asapambane pa nkhondoyo ngati m'mene anaŵawuzira. Chomcho anali opanikizika kwambiri.